Baibulo ya ana
Ikupasilani

Yakobo Wonyenga

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: M. Maillot; Lazarus Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: M. Kerr; Sarah S.

Yotanthauzilidwa ndi: Tapiwa Maraira

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Kodi Mulungu anatumizapo mwana ku banja lanu? Zosangalatsa bwanji! Isake ndi Rabeka ayenera kuti anasangalala kwambiri. Mulungu ankati adzawapatse
iwo mapasa.

Anawo ankavutikira m'mimba mwa Rabeka. Pamene ankapemphera, Mulungu ananena kuti ana ake aamuna awiri adzatsogolera mitundu iwiri, ndipo wamng'onoyo adzakhala wamkulu. Nthawi zambiri, woyamba kubadwa anali wamkulu. Pomalizira pake anawo anabadwa.

Mapasawo sanali ofanana. Esau, yemwe anali wamkulu, anali ndiubweya wambiri ndipo anakula kukhala mlenje waluso. Yakobo anali ndikhungu losalala komanso amakonda kugwira ntchito kunyumba. Atate Isake ankakonda kwambiri Esau. Amayi ankakonda Yakoko

Tsiku lina Esau anamva njala. Iye anauza Yakobo kuti: “Ndipatse chakudya.” “Ndikulitsire ukulu wako,” anafunsa motero Yakobo. Esau sanasamale malonjezo a Mulungu kwa ana oyamba kubadwa. Anapangana ndi Yakobo. Tsopano Yakobo ndiye anali kukhala mutu wa banja bamboo awo atamwalira.

Mulungu analankhula ndi Isake usiku wina. "Ine ndine Mulungu wa atate wako Abrahamu. Ine ndiri ndi iwe, ndipo ndidzadalitsa mbewu yako." Ngakhale kuti Isaka ankalambira Mulungu, mwana wake Esau anakwatira akazi awiri a Ahiti, anthu amene sankakhulupirira Yehova.

Isake anakalamba.
Iye anauza Esau kuti: “Chonde undibweretsere nyama yatsopano. Ndiye ndidzakudalitsa iwe.”
Dalitso lapadera limeneli linali kuchokera kwa atate kupita ku mwana woyamba kubadwa. Esau anathamanga kukasaka. Koma Rabeka anamva. Iye ankafuna kuti Yakobo adalitsidwe.

Rabeka anali ndi dongosolo. Pamene ankaphika mwamsanga chakudya chimene Isake ankachikonda, Yakobo anavala zovala za Esau n'kumuveka zikopa zaubweya m'manja ndi m'khosi. Isake sanaone bwino. Mwina akanamukanira.

Yakobo anabweretsa chakudyacho kwa Isaka. "Iwe ukumveka ngati Yakobo," Isake anati, "koma manja ako afanana ndi Esau." Atadya chakudyacho, Isake anadalitsa mwana amene anagwada pamaso pake.

Yakobo atangochoka, Esau anafika kwa Isaka. "Chakudya chako ndi ichi," adatero. Isake anadziwa kuti wapusitsidwa. "Sindingathe kusintha dalitso," adalira. Mtima wa Esau unazadza ndi chidani. Anaganiza zopha Yakobo.

Rabeka anamva kuwopyeza kwa Esau. Iye anauza Yakobo kuti: "Pita ku nyumba ya amalume ako, mpaka mukulu wako aiwale zimene unachita." Isake anavomera kuti Yakobo afunefune mkazi wa banja la amayi ake. Chotero Yakobo anachoka panyumba.

Usiku umenewo,
Yakobo anagona
ndi mwala woika mtsamiro.
Mwina anali yekhayekha,
mwinanso mantha. Koma
sanali yekha. Mulungu
analankhula naye
m'maloto
odabwitsa.




"INE NDINE MULUNGU
WA ATATE ANU, ABULAHAM NDI ISAAKA.
NDINE NDI IWE. NDIDZAKUPATSA DZIKO
LINO. NDI BANJA LAKO MABANJA ONSE A
PADZIKO LAPANSI ADZADALITSIDWA."
Mulungu atalankhula, Yakobo anadzuka.
Iye anachita mantha.

Labani amalume ake a Yakobo anamulandira bwino. Yakobo anakonda msuweni wake Rakele ndipo anatumikira Labani zaka zisanu ndi ziwiri kuti akwatire iye.
Koma, usiku wa ukwati, Labani anamunamiza Yakobo.

“Uyu ndi Leya, osati Rakele,” anadandaula motero Yakobo. “Mwandipusitsa.” Labani anati, “Mwana wamkazi wamkulu akwatiwe kaye. Ukwatirenso Rakele, ndipo unditumikire zaka zina zisanu ndi ziŵiri.” Yakobo anavomereza, mwinamwake anakumbukira chinyengo

chimene iye mwini anachitira Isake ndi Esau.

Yakobo anali ndi ana amuna khumi ndi mmodzi. M'kupita kwa zaka analakalaka kutenga banja lake kubwerera ku Kanani. Makolo ake analipo.

Koma Esau analumbira kuti amupha. Kodi zinali zotetezeka? Tsiku lina Mulungu anamuuza kuti abwerere. Yakobo anasonkhanitsa banja lake ndi ziweto zake kuti apite kwawo.

Unali ulendo wotani. Esau anabwera kudzakumana ndi Yakobo ndi amuna mazana anayi! Koma sanamupweteke Yakobo. Anathamanga kukakumana ndi Yakobo ndipo anamukumbatira. Yakobo ndi Esau analinso mabwenzi,
ndipo Yakobo anali panyumba.

Yakobo Wonyenga

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Genesis 25-33

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mumtima mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16